Mphanvu Yo Dabwitsa Ya Dalitso

Richard Brunton

Mphanvu Yo Dabwitsa Ya Dalitso

Richard Brunton

Mphanvu Yo Dabwitsa Ya Dalitso
Otulutsa ndia Richard Brunton Ministries
New Zealand

© 2018 Richard Brunton

ISBN 978-0-473-46092-1 (ePUB)
ISBN 978-0-473-46093-8 (Kindle)
ISBN 978-0-473-46094-5 (PDF)

Kukonza:
Kuyamika kwa padela kwa
Joanne Wiklund and Andrew Killick
po panga nkhaniyi kuti yiwerengeke bwino
kuposa mwina mwache m'mene idaka khalira!

Kupanga ndi kukonza bwino:
Andrew Killick
Castle Publishing Services
www.castlepublishing.co.nz

Luso la chakubwaro:
Paul Smith

Mau yo patulika ya tengedwa mu
King James Ya Tsopano mbali®.
Bene bake © 1982 na Thomas Nelson, Inc.
Yisebenzetsedwa ndi chivomerozo.
Danga Silinapatsidwe.

DANGA SILI NAPATSIDWE

Kulibe mbali ya buku iyiyimene yinga pa ngidwenso,
kapena kusungidwa mu njira yiri yonse, kapenaku wulitsidwa
mu njira yili yonse muli chinthu chili chonse, mu va malaiti, makina,
ku kopera, ku yika pa makina kapena mu njira yili yonse,
popanda chirolezo ku chokera kwa eni aka ana tu;lutsa bukulu.

ZA M'KATIMU

Mau Yoyamba 5
Choyamba 9

Gawo lo yamba: N'nchifukwa ninji Dalitso? 15
Mphunzilo 17
Mphanvu Yili M'zokamba Zathu 21
Kuchokela Kukamba zabwino ndi kuyamba ku Dalitsa 24
Dalitso ya UKlisitu ndi Chani? 27
Ulamuliro wanthu Wa Uzimu 31

Gawo la ciwiri: Mochitila 39
Zochita zina zo Funikila 41
- Lekani kamwa koyela kakhale umoyo anu 41
- Funsa M'zimu Woyela zokamba 41
- Kudalitsa kusiyana ndi ku pemphelerana 42
- Usaweluze 43
- Chitsanzo cho wonetsela 44

Zochitika zomwe Tingakumane Nazo 47
- Kudalitsa iwo okunyozani ndi kukutembelerani 47

Kudalitsa okupweteka ndi wokukana 48
Kudalitsa iwo wokuyambani 51
Tidalitse, Tisadzitembelere Tekha 55
Kuzindikila ndi kuwononga matembelero 55
Kudalitsa kamwa kanu 58
Kudalitsa maganizo yako 59
Kudalitsa mathupi yahu 60
Kudalitsa nyumba yanu, chikwati ndi ana 65
Dalitso ya atate 74
Kudalitsa ena pa ku lamkhula chinenelo 79
Kudalitsa malo yatchito yanu 80
Kudalitsa m'malo omwe tikhalamo 83
Kudalitsa nthaka 85
Kudalitsa Ambuye 86
Mau yo tsilizila yo chokela ku wowerenga 87

Zochita 89
Momwe mu Ngakhalire m'Klisitu 91

MAU YOYAMBA

Niku limbitsani kuwerenga buku ling'onoli ili ndi uthenga wa mphanvu – muzasithidwa!

Linari pamene ine ndi Richard Brunton tinali kudya chakudya cha m'mamawa m'mawa mwinapamena iye anandi uzako zimene Mulunguana nvumbulutsira pa za mphanvu ya dalitso, ndipo mosataya nthawi ndi nawona zimene zinalimo kuti zingasithe myoyo ya anthu ena.

Ndinajambula uthenga wake kuti ndikawonetse ku mpingo wathu ku m'sonkhano wa azibambo. Azibambo analipo pam'sokhanowu anawona kuti chinali chabwino kuwonetsa m'pingo onse kuti unvereko chifukwa uthenga unali wabwino. Anthu anayamba kusewenzetsa mu mbali iriyonse ya umoyo wawo ndipo tina nvera maumboni yo zizitsa chifukwa chazimenezi. M'zibambo wina wa malonda

ananena kuti malonda yake yana chokera 'palibe-libe, ndikuyamba kupanga pindu' mumasondo yawiri. Yena anachiritsidwa m'thupi pamane anayamba ku dalitsa mathupi yayo.

Maumwayi ena ya uthenga uyu yaza nvedwa yinayamba ku tseguka. Ndinari kuyembekezeredwa ku kalakhura ku guru la Kusokhana la Akuru-Akuru (komwe azibusa amipingo ana bwera pamozi kuphunzira ndi kusitsimutsidwa) ku Kenya ndi ku Uganda. Richard anapita nane pa ulendowu nalakhurapo pa gawo la dalitso. Uthenga una fukulura zopandapache ndi zowawa zina fochelewa kale. Anthu ambiri m'guru sanadalitsidwepo ndi makolo awo ndipo pamene Richard anayimilira nawadalitsa, ambiri analira ndikunvera chimasuko m'maganizo ndi pauzimu ndi kusintha myoyo yawo mwa msanga.

Kuziba kudalitsa kwa sintha umoyo wanga kufikira pakuti ndifunafuna umwayi odalitsiramo ena mu 'mau ndi zochita' – kupitira zomwe ndi kamba ndi kuchita. Muzakanvera bwino aka ka buku kang'ono, ndipo mukazichita mu umoyo wanu, zipatso zimene

muzabala ziza khalirila ndi ku tayikira mu ufumu wa Mulungu.

Geoff Wiklund
Geoff Wiklund Ministries,
Wa kumphando, Promise Keepers,
Auckland, New Zealand

Mulungu adalitsa Richard na chibvumburutso cha mphavu ya dalitso pamene imasulidwa pa ena. Ndikhulupilira kuti yichindi chi bvumbulutso cho chokera kwa Mulungu cha nthawi yathu.

Pamene Richard achita zili mu uthenga wake, anthu mwa m'sanga-m'sanga alinganiza ndi mwine wake.

Yichi chinalengesa kuti tiyitane Richard kuti azakambe pa misonkhano ya azibambo anthu ya'Promise Keepers'. Zo nvekamo zinali za mphanvu yayikulu ndiponso zo sintha-moyo kwa anthu ambiri.

'Dalitso' unali mutu wankhani umene unafika ndi

kutenga mitima za anthu m'misonkhano ya Promise Keepers. Kunali ku vomereza kwa bwino kwa kukuru kwa uthenga wofunikilawu – dalitso, kulankhula dalitso ndi mphanvu ya 'kukamba zabwino'. Azibambo ambiri sanalandirepodi dalitso kapena kuyipatsa ku ena. Atanvera uthenga wa Richard, ndi kuwelenga buku iyi,analandira dalitso larikulu ndipo anapatsidwa kuti adalitse ene mu zina la Atate, ndi Mwana ndi M'zimu Woyera.

Ndikamba za bwino kwa Richard ndi buku iyi *Mphanvu Yo Dabwitsa Ya Dalitso* ngati njira ya mphanvu yo masula kadzadzidwe ka dalitso ya Mulungu m'mabanja mwanthu, mwamene tikhala nai m'dziko la thu.

Paul Subritzky
Mkuru wa Dziko lonse, Promise Keepers
Auckland, New Zealand

CHOYAMBA

Aliyense amakonda ku nvera uthenga wabwino – ndipo ndichabwino ngati ndiwe wa ulutsa!

Pamene ndinazindikira wopata dalitso, chinali ngati kuti ndine uja munthu wa m'Baibulo omwe adapeza zam'tengo wapatali m'munda. Mosangalara ndinthu ndina gawirako maganizo yanga ndimomwe ndinali kunvelera ndi m'busa Geoff Wiklund ndipo anandiuuza kuti ndilankhure kwa azibambo amum'pingo wawo pa m'sonkhano wa mwezi wachiwiri wa mu 2015. Uthenga unawakondweletsa kwambiri kwakuti anafuna kuti m'pingo wonse uwunvere.

Pomwe n'nalakhula pa m'pingo, Opatsidwa ulemu a Brian France, aku Charisma Christian Ministries, ndi Paul Subritzky, aku Promise Keepers NZ, anali mu m'sokhanowo. Ichi chinalengetsa kuka gawanitsa uthengawu ku Charisma ku New Zealand ndi ku Fiji, ndi kwa a zibambonso aku Promise Keepers.

Ambiri anawutenga uthengawu ndiku wu sewenzetsa mwam'sanga-m'sanga ndizoturukamo zabwino zinawokela. Ena analakhula kuti sana nvelepo kumbuyoko chiphunzitso cha iyi mbariya ufumu wa Mulungu.

Utumiki wa dalitso unakura kwa mbiri (Kodi Mulungu sanalakhule, 'Mphatso yamunthu yizda m'ziwitsa iye kuanthu'?) Kumathelo kwa chaka cha 2015, ndina pelekeza m'busa Geoff ku Kenya ndi ku Uganda. Anali kutumikila uthenga ku mazana ya azibusa omwe anasonkhana pam'sonkhano wa akulu-akulu. Kusonkhanaku kunali kwa pa chaka komwe iwo osonkhanawo ana bwera kulimbitsidwa ndi ku thandizidwa, ndipo Geoff anaona kuti chiphunzitso change pali dalitso chingakhale chowathandiza iwo. Ndipo china chitika choncho. Sazibusa okha, koma ndiolakhula ena ochokela ku America, Australia and South Africa anaona kuti unali uthenga wa mphanvu ndipo ana ndilimbitsa kuti ndichitepo chimodzi kuti uthengawu ufike kuanthu ambiri.

Sindinafune kupanga ndi ku sunga webusaiti, kapena kulemba mwadongosolo ntchitoyi pomwe

zolembedwa zina zopandana zilipokale. Uthenga wa dalitso ndiwapafupi – usewenzesedwa bwino-bwino – ndipo sindinafune kuti kufupikaku kusowe m'kutaliphitsa – n'chifukwa chache uli m'kabuku kang'ono aka.

Ndatenga mau kuchokelamu *Mphanvu ya Dalitso* ya Kerry Kirkwood, Kuthilidwa kwa Chisomo*: Kukhala anthu a Dalitso elemba ndi* Roy Godwin ndi Dave Roberts, *Dalitso ya Atate olemba ndi* Frank Hammond, ndi *Choziziswa ndi Mphanvu ya Dalitso olemba ndi* Maurice Berquist. Ndikulupilira kuti ndatengamo kapena kumphunzira kwa anthu ena ndi mabukunso ena, koma pa zaka izi chiphunzilochi cha gumikuzana.

Kuzindikira mphanvu ya dalitso kwa tsegula njira yatsopano yonkhaliramo kwa munthu aliyense amene ayisewenzetsa. Ndidalitsa anthu masuku ambiri tsopano – wokhulupilira ndi wosakhulupiira – momwera, modyera, mofikira alendo, mopumulira ndi m'misewu. Ndadalitsa ana amasiye, osewenza m'yumba za ana amasiye, m'zimayi osewenzera mu ndeke pa ndeke, m'madimba, zoweta, mosungila ndalama, zogulitsa ndiwo sanvera bwino. Ndakhala

ndili ku khala ndi a zibambo ndi azimai akulu-akulualikulira pa chifuwa change pomwe ndiku lankhula dalitso la Atate kwa iwo.

Pamene ndi kulankhula ndi wosakhulupilira, ndapeza kuti 'Nikudalitse/malonda yako/chikwati chakondizina zotelo?' sichinvesa mantha kwambiri kuposa'ndikupephelere?' Indetu, kuchita motele, kochitidwa m'chikondi cho khuzidwa, chinalengetsa m'modzi wa m'banja mwanga kuziwa chikond ndi mphanvu ya chipulumutso cha Ambuye Yesu, patapita zaka zambiri zotsutsana.

Nthawi zambiri sindimaona zochokamo, koma ndawona zambiri kuti niziwe kuti dalitso limasintha myoyo. Ndipo la sintha umoyo wanga inenso.

Ndi uMulungu wa Mulungu kudalitsa, ngati wolengedwa m'chifanizo chake, chili mu uzimu mwanthunso naisenso. M'zimu Woyela ali kuyembekeza anthu a Mulungu kuti apite m'chikhulupiliro ndi mu ulamuliro wa Yesu Khlistu womwe anapatsidwa kuka sintha myoyo.

Ndili wokhutila kuti muzapeza thandizo mulu kabuku kang'onoka. Yesu sanatisiye tilibe mphanvu. Kulankhula madalitso mu zonse zo

chikitika ndi chisomo cha uzimu chimene chalekeleredwa chimene chili ndi mphanvu yo sintha dziko lanu.

Nvelani bwino.
Richard Brunton

GAWO LO YAMBA:

N'nchifukwa ninji Dalitso?

MPHUNZILO

M'kazi wanga Nicole niwaku New Caledonian ndi ichi, inde, ndinafunika kumphunzira kulankhula chitundu cha French ndi kutengako nthawi ndithu kukhala kumalo anabadwira, Noumea. Ngakhale kutidziko la New Caledonia ambiri ndi a Catolika, sipanapite nthawi nikalibe kuziwa kuti anthu ambiri anali ku tengako mbari mu 'za mu m'dima', pamenenso anali kucita chipembezo chawo. Sichinali cho bvuta kuwona anthu kupita kuka wombeza, kuwona amizimu popanda kuzindikila kuti anali kufunsa nfiti.

Ndikumbukila m'kazi wanga pomwe ananditenga kupita kuka wona m'zimayi wa chichepele m'mazaka za makhumi yawiri emwe anapelekedwa ku amodzi a awa 'wo poletsa', koma iye, zitachitika zomwezi, anazipeza kuti apelekedwe ku nyumba ya anthu osokonezeka m'zeru kapena anthu odwala m'maganizo. Pomwe ndinaziwa kuti ndi m'Khilisitu, ndinalamulira ziwanda zomwe zidakamulowa kuti

zituluke, muzina la Yesu Khlistu. M'bambo wa Catolika anapephela nayenso ndipo, pakati pathu ise, uyu m'tsikana anamasulidwa ndi ku m'tulutsa m'chipatala chija pasana pite nthawi yayitali.

Ena anabvomeleza chipembezo cha Catolika chayo komanso anali kuwonetsa mafano ndi zopanga zazipembezo za milungu ina.Kunali muthu wina omwe ndina kumana naye emwe anali ndi vuto ya m'mimba yopitilira. Tsiku lina ndinati kwayiye kuti ndikhulupilira kuti akataya chi Buddah chachikulu, chonenepa chiri ku tsogolo ya nyumba yake – chinali kuyaka usiku – mavuto ya m'mimba mwake yaza-tha. Mowonjezelapo, vowumba vachipembezo vina vomwe anatenga vina funika kuti vipite. Analimba – kodi naga ivi va 'kufa' vinthu vinga mu dwazike bwanji? Patapita mwezi ndinamuwonanso ndipo ndina mufunsa kuti m'mimba mwake mulibwanji. Monga mwa manyazi anati, 'Ku matsiliziro ndina tenga nzeru ya wunandipatsa ndipo ndina taya Buddha. M'mimba mwanga mulibwino tsopano.'

Pa nthawi yina, anandipempha kupita ku nyumba ya m'zimayi analikudwala matenda ya kansa. Ndikalibe

kuyamba ku kupemphera ndi nawawuza kuti ataye mafano ya Buddha m'nyumba mwawo, ndipo mwamuna wake anachichita mwam'sanga-m'sanga. Pamene ndinali kuwononga matembelero pali iye ndipo ndinalamulira bvibanda kuti bvi choke mu zina la Yesu, anati chozizilachinali kuyenda m'thupi mwake kuchokela ku minyendo ndi ku tulukila ku mutu.

Mwa ichi, kulinga ndi zimenezi, ndinaganiza ku phunzitsa pa 'matembelero' ku guru ya mapemphero yimene ine ndi m'kazi wanga teze tinayamba m'nyumba yathu ya ku Noumea. Chiphunzitso chinachokela mu zolemba za Derek Prince (Derek Prince anali m'phunzitsi wodziwika wa Baibulo wa mazaka akumbuyo). Pamene ndinali kukonzekera uthenga wanga m'chitundu cha French, ndinaphunzira kuti liwu lawo la mawuakuti kutemeblera linali lakuti *malédiction*, ndipo liwu lao lakuti dalitso linali *bénédiction*. Chiyambi cha mau awa ndi 'kukamba zoipa' ndi 'kukamba zabwino'.

Kalero, pamene ndinali kulinganizakutembelera ndi kudalitsa, kutembelera kunali kuwoneka kwa

kuda, kolema ndi kowopsa, ndipodalitso inawoneka yo pepuka. Ndinanvela zimphunzitso pa kutembelera kumbuyoko, koma osati pa dalitso – ichi mwina mwache chinalengesa kuwona kwa zinthu kumeneku. Sindinanvelepo wina munthu kudalitsa munthu winamwa mphanvu ndi lingo la bwino. Ndipo, chifikiro cha dalitso ya chi Klisitu imakhala chabe yonena kuti 'Udalitsidwe', pamene wina wa wa nvera chinfine, kapena kulemba 'Madalitso' po tsiliza kalata – monga ngati kuti ndi m'khalidwe osati chitu chochita ndi ganizo.

Nthawi yina, pamene ndinali kuganiza aya mau, 'malediction' and 'benediction',ndinazindikila kuti ngati 'kukamba zoipa' kunali ndi mphanvu, ndiye kuti 'kukamba zabwino' kuyenekelanso nako kukhala ndi mphanvundipo, ndi Mulungu, kuyenera ku khala ndi mphanvu yayikulu!

Chibvumbulutso chimenechi, pamodzi ndi zo mpunzira za m'kati ziza kambidwa kusogolo, zina lengetsa kuti ndi yipeze mphanvu ya dalitso.

MPHANVU YILI M'ZOKAMBA ZATHU

Kusafuna kubwezapo zomwe mabuku yambiri yabwino yanakambapo kale pa za mphanvu ya mau athu, ndifuna kupatsa dogotsolo pango'no pazimene ndikhulupilira kuti ndizofunikira kumbari yimeneyi.

Tidziwa kuti:

> *Infa ndi moyo ziri m'phanvu ya lirime ndipo iwo amene ayikonda, azdadya zobala zake. (Miyambo 18:21)*

Mau yali ndi mphanvu yayikulu – pena yabwino yo manga zinthu, komanso yoyipa yowononga zinthu. Nthawi yiliyonse yimene tilankhula mau (ndipo munjira yiliyonse yimene tiya sebenzetsa, yimene yipatsa tanthauzo ku mau), timalakhula infa kapena moyo kuli iwo otinvela ndiponso kwaisenso. M'kupitiliza, tiziba kuti:

> *Zochokela za pansi pa mtima kamwa kama-zilakhula. Munthu wa bwino kuchokela mzabwino zamu mtima wache abweletsa zinthu zabwino, ndipo munthu woyipa kuchokela m'zoyipa zache ambweletsa zinthu zoipa. (Mateyo 12:34-35)*

Nchifukwa yichi, kuchokela mu mtima otsutsa lirime lotsutsa limalakhula; kuchokele mu m'tima woziyetsa-wekha, lirime la chiweruzo; m'tima wosayamika, lirime la madandaulo; mpaka telo. Chimodzimodzi, mitima zolakalaka zibala zipatso zake. Dziko ndilo dzadzidwa ndi kakambidwe koyipa. Wofalitsa uthenga azikamba tsiku ndi tsiku. Munthu akhala momwe aliri, sitimakamba zabwino pali anthu kapena zomwe zichitika. Sichimabwela chekha kuli yise. Nthawi zambiri timayembekezera banthu bafa tikalibe kukamba zabwino za iwo. Zingakhale telo 'zabwino' zichokela mumitima za chikondi zimene zizakamba ndi lirime la chisomo; kuchokela m'mitima ya mutendere, lirime yokhulukilira; mpaka choncho.

Mndandamiko wa mau, 'ndipo iwo amene ayikonda, adzadya zipatso zake' yasonyeza kuti tidzakolora

zimene tibzala – kapena zabwinokapena zoipa. Kapena kuti, uzakhala ndi zimene ulakhula. Kodi muganiza chiyani pali zimenezi?

Ichi nichoonadi kwa munthu aliyense, ngakhale kuti akhulupilira za Uklisitu kapena iyai. AKlisitu ndi iwo amene sali Aklisitu chimodzimodzi akamba mau ya umoyo – mwa chitsanzo, wina angati: 'Mwana wanga, ako ka nyumba komwe wa manga ndi kabwino. Uzakhala wopambana m'kumanga manyumba kapena wolemba zakamangidwe tsiku lina. Wachita bwino.'

Zingakhale tero, M'Klisitu wo badwa kwa sopano ali ndi mtima wa tsopano. Baibuloinachiyika motele kuti ndise 'chilengedwe chatsopano' (2 Akolinto 5:17). Mwayichi, ngati AKlisitu, tiyenela kukamba zabwno zambiri ndipo zoipa zazingo'no. N'chapafupi kuyamba kukamba zoipa ngati sitikhala atchelu ku samalira mitima zanthu ndi mau athu. Ukayamba kukhala wozindikila pali zimenezi, uzadabwa momwe AKlisitu nthawi zonse – ngakhale m'kusadziwa – amadzitembelera okha ndiponso anzawo. Zambiri pali izi zizakambidwa bwino.

KUCHOKELA KUKAMBA ZABWINO NDI KUYAMBA KU DALITSA: NDI MAYITANIDWE YATHU

Monga AKlisitu, tilina umoyo wa a Mbuye Yesu ulikuyenda mwayise, tinga pitilire pazakukamba zabwino chabe – tingakambe ndikubweretsa madalitso ku anthu kapena kulizimene zichitika – ndipo ndizoona tinayitanidwa kuchita chimenechi. Mwina mwache kudalitsa ndi mayitanidwe yathu ya akulu. Werengani izi:

> *Khalani wokomerana m'tima, lemekezanani; osabweza choipa ndi choipa kapena kunyoza pa kunyoza, koma munjira ina dalitsani, pozindikira kuti munaitanidwa kuli chomwechi, kuti mukalandire dalitso. (1 Peturo 3:8-9)*

Ndise oyitanidwa ku dalitsa ndi kulandilitsa dalitso.

Choyamba chimene Mulungu analakhula kwaAdamundi Eva chinali dalitso:

> *Ndipo Mulungu anabadalitsa, ndipo Mulungu anati kwa iwo, 'Balani ndipo chulukani; dzadzani dziko lapansi ndipo lilamulireni…' (Kuyamba 1:28)*

Mulungu anabadalitsa kuti abalane. Dalitso ndi mbali ya uMulungu – ndiye chimene achita! Nipo ngati Mulungu – ndiponso wochokela kwa Mulungu – nainsenso tili nawo ulamuliro ndi mphanvu za ku dalitsa ena.

Yesu anadalitsa. Cho tsilizila chimene anachita, ngakhale pamene anali pafupi kupita ku mwamba, kunali ku dalitsa ophunzira ake:

> *Ana pita nawo kufikila ku Bethani, ndipo ana nyamula manja yake nawa dalitsa. Tsopano chinachitika, pamene anali kubadalitsa, anasiyana nawo iwo na nyamulidwa kupita ku mwamba. (Luka 24:50-51)*

Yesu ndiye owonelako wathu. Anati kuti tikazichita zimene iye anachita, muzina lake. Tayikidwa ndi Mulungu kuti ti dalitse.

DALITSO YA UKLISITU NDI CHANI?

Muchipangano Chakale, mau akuti 'dalitso' ndi mau ya chi Heberi yakuti *barak*. Ichi chitanthauza kuti, 'ku kamba zomwe Mulungu aganiza'.

Muchipangano Chatsopano, mau yakuti 'dalitso' ndi mau ya chi Giriki yakuti *eulogia*, komwe tichotsa mau yakuti 'eulogy'. Mwa yichi, m'kuchita, ichi chitathauza kuti 'kukamba zabwino' kapenanso 'kukamba malingaliro ndi kukoma mtimakwa Mulungu' pa munthu.

Icho ndiye chikambidwe cha dalitso chimene ndidza sewenzetsa m'bukuli. Dalitso ndi kulankhula maganizo ndi kukoma mtimakwa Mulungu pa munthu wina kapena muzochitika.

Mulungu, kwa nthawi yitali, mu nzeru zake, anaganiza kuti nthito yake pano pa ziko asebenzele muli banthu bake. Ndi njira imeneyi mumene abweretsa

ufumu wake pano pa ziko lapansi. Chimodzimodzi, afuna kuti tikazidalitsa anthu m'malo mwache. Mwa ichi,ngati Mklisitu, ndingalakhule nganizo laMulungu ndi chisomo chake pa munthu kapena pazochitika muzina la Yesu. Nikachita zimenezi ndi chikhulupiliro ndi chikondi, ndiyekuti nizakhalanayo mphanvu ya kumwamba kuti yichite zonse zomwe nilankhula, ndipo ndingayembekezere Mulungu ku sintha zinthu kuchokela momwe ziliri ndikuzipereka momwe iye afuna kuti zikhaliremo. Ngati ndifuna kudalitsa wina, ndi chikondi ndi chikhulupiliro, ndichititsa kuti zolinga za Mulungu zichitike pa munthu uja.

Kumbari yina, munthu wina mwadala, kapena kwa nthawizonse mosaganiza bwino, alankhula maganizo ya satana pa umoyo wamunthu, kapena pa umoyo wawo, chimene chimalengetsa kuti mphanvu za adani kuti zichite zolinga zawo pa umoyo wamunthu uja – uku ndi, kuba, kumpha ndi kuwononga. Koma Mulungu atamandidwe,

> *Iye ali muli inu ndi wa mkulu kupambana iye ali mu ziko lapansi (1 Yohane 4:4).*

Mtima wa Mulungu ndiwofuna Ku dalitsa – ndithudi ndiye mwaliri! Chilakolako cha Mulungu ku dalitsa nchancikulu modabwitsa. Palibe chingamuletse. Iye anayimilira kudalitsa anthu. Afuna kuti Yesu akhale ndi abale ndi alongo ambiri. Ndiwo ise! Koma, pamene chili mu m'tima wa Mulungu ku dalitsa anthu, iye afuna kuti anthu ake azidalitsana.

Pamene tidalitsa m'zina la Yesu, M'zimu Woyela umabwera chifukwa tiwonetsa zimene Atate achita – tikamba mau yomwe Atate afuna kuti azikambiwa. Nimadabwitsiwa nthawizonse pa choonadi ichi. Tikadalitsa wina, M'zimu Woyela adalitsako – Akhuza munthu uja, chikondi chimasulidwa ndipo vinthu vichinja. Nthawi zonse anthu amandikumbatila pot-satila zimezi naati, kapena amalira naati, 'Siwudziba kuti uthengawu wafika pa nthawi yake ndi momwe mphanvu yake mwailiri', kapena 'siwudziba mwamene ndinali kuufunira uthengau'.

Koma pali china chofunikira kwambiri chomwe chi-funikira kudzibika: timadalitsa pomwe tilipamozdi ndi Mulungu, kuchokela m'malo mwake. Kukhala pafupi ndi Mulungu muuzimu wathu ndi chofunikila

kwa mbiri. Mau yathu ndi mau yake ndipo ndiyo-zozedya ndi mphanvu yake kuti yachite chifunilo chake cha munthu uja kapena zochitika. Koma tiyeni tipeleke umboni pang'ono…

ULAMULIRO WANTHU WA UZIMU

Mu chipangano chakale, ba ansembe anali ku pemphelera anthu ndi kulankhula madalitso pa iwo.

Umu ndimo uzadalitsila ana a Israeli. Kamba kwa yiwo kuti:

Ambuye akudalitse ndi kukusunga;
Ambuye asanike nkhope yake pali inu,
ndipo akukomereni m'tima.
Ambuye anyamule nkhope yape pali inu,
ndikukupatsani mtendere.

M'menemu adzayika zina langa pa banaba Israeli,ndipo ndizabadalitsa. (Numbers 6:23-27)

Mu chipangano cha tsopano, ise ngati AKlisitu titchedwa kuti:

> *M'badwo osankhidwa, ansembe akuufumu, zdiko loyela, anthu ake apadela, kuti mulankhule matamando yake iye yemwe anakuyitanani kuti muchoke ku m'dima ndiku bwela mu nyali yake yodabwita. (1 Peturo 2:9)*

Ndipo Yesu anati

> *…atipanga ise mafumu ndi asembe kwa Mulungu ndi Atate… (Chibvumbulutso 1:6)*

Nthawi yina kale, n'nali khale pansi pa Ouen Toro, yoyang'anila mu Noumea, kufunafuna uthenga okalalikira ku guru ya mapemphelo.Ndina ganiza kuti Mulungu alankhula kuti, 'Simudziba kuti ndimwe ndani.' Ndipo mwezi itapitapo: 'm'dakaziba ulamuliro muli nawo mwa Yesu Kilisitu m'daka sintha ziko lapansi.' Mau thenga ya wiliriwa anali ya maguru ena ya anthu, koma, ndinazindhikila kuti, yanali yanganso.

Ndiganiza ndi chozibika mu chi Kilisitu kuti kulankhula ku matenda kapena ku zochitika (phiri – Mako 11:23) ndikulamulira machilitso chimasebenza bwino kuposa kupempha Mulungu kuti akuchitile

chomwecho (Mateyo 10:8; Mako 16:17-18). Izi ndizo zomwe naona ndi kuzipitamo ndiyena ambiri opatsidwa ulemu ndi okwanitsa zinthu mu utumiki wama chilitso ndi chiwombolo. Ndinkhulupilira kuti Yesu anatanthauza ichi, 'Chilitsani odwala (m'zina langa). Sitchito yanga, nditchito yanu. *Yigwireni*.'

Mulungu afuna ku chilitsa ndipo afuna kuchilitsa kupitila muli ife. Mulungu afuna kuwombola ndipo afuna kuwombola kupitila muli ife. Mulungu afuna kudalitsa ndipo afuna kudalitsa kupitila muli ife. Tinga mpemphe Mulungu kuti adalitse, komanso tinga dalitse muzina la Yesu.

Zaka zapita kumbuyo, ndikumbukila pomwe ninapita ku tchito mwamsanga kukadalitsa malonda anga. Ndinayamba kuti, 'Mulungu, dalitsa Colmar Brunton.' Sindinanverepo chilichonse. Ndipo ndinasintha – mwa manyazi pang'ono pachiyambi – kuchokela kuti 'Mulungu dalitsa Colmar Brunton' ndikukamba kuti:

> *Colmar Brunton, ndiku dalitsa muzina ya Atate, Mwana ndi M'zimu Woyela. Ndikudalitsani inu muno Auckland, ndipo ndikudalitasni inu muno*

mu Wellington, ndipo ndikudalitsani m'madela. Ndiku dalitsani pa tchito ndipo ndikudalitsani pa nyumba. Ndimasula Ufumu wa Mulungu m'malo yano. Bwela M'zimu Woyela, Ndiwe olandilidwa pano. Ndimasula chikondi ndi Chimwemwe ndi mtendere ndi kudekha ndi chifundo ndi kukoma ndi kuleza m'tima ndi kuziletsa ndi kugwirizana. Muzina la Yesu, ndi masulazoganiza zo coka mu ufumu wa Mulungu zomwe ziza nthandiza omwe tichita nawo malonda kuti azipambana ndi panga ziko lapansi malo abwino. Ndi masula kukoma mtima kuwomwe tichita nawo malonda. Ndimasulo kukoma mtima m'malo wolemba tchito. Ndidalitsa maso mphenya yathu: 'Malonda yabwino, dziko lapansi labwino'. Muzina la Yesu, amen.

M'mene ndinavera kutsogozedwa, ndinali kupanga mtanda ndi manja pakhomo ndi ku lakhula muuzimu chichingilizo cha mwazi wa Yesi pa malonda yathu.

Kuchokela pomwepo ndina sintha kuchokela kukamba kuti 'Mulungu dalitsa Colmar Brunton'

mkukamba kuti 'ndi dalitsa Colmar Brunton mu zina la Atate ndi Mwana ndi M'zimu Woyela', mzozo wa Mulungu unagwa pali ine – ndinanvera kuti Mulungu alinaine ndipo andi vomekeza. Chinali monga anali kukamba kuti, 'Ulinacho, mana wanga mwamuna; ndiye chimene ndifuna kuti ukazichita.' Ngakhale kuti ndachita zimenezi kwa kathawi ka mbiri, ndakhala ndili ku nvera nthawi zonse chifunilo cha Mulungu muzimenezi. Ndipo zochokamo? Kachitidwe kazinthu m'malo yosebenzera kanachinja, ndipo kana chinja mwa msanga, kufikila pa nthawi yakuti anthu anayamba kuzikamba osati mwa kabisila, ndi kudabwa nchifukwa ninji zinthu zinasintha. Chinali chodabwitsa! Dalitso nzoonadi lingasithe ziko lathu.

Koma sindinalekele pomwepo. M'mawa, pomwe anthu akalibe kubwera pa tchito, ndikafika pa mpando wa munthu uja analikufuna nzeru pa zomwe anali kuchita, ndinali ku adalitsa, kuyika manja yanga pa mpando wawo, ndikunkhululupira kuti mzozo okwanilitsa dalitso udzapita mu mpandowo ndiku fika kuli uja muntu emwe akhala pomwepo (Machitidwe 19:12). Ndikazindikila chabe zomwe munthu akufuna,ndinali ku dalitsa mu njira imenewo.

Ndikumbukila munthu wina anali ndi khalidwe lo nyoza – chakuti, analikusebenzetsa zina la Mulungu ndi ukaliwake. M'mawa mwina ndinayika manja yanga pa mpando wake, ndikumanga m'zimu wa manyozo, mzina la Yesu. Chinatengako nthawi, koma nthawi yinafika pomwe mzimu oyipawo unagonja pa nkhongono ku mphanvu yayikulu ndipo mzimu wonyoza uja unachoka mzokamba za uja munthu patchito paja.

Ndikumbukilanso munthu wina emwe anabwera kuli ine kuti ndi mpepherele, analikufuna Mulungu kuti amuchosepo pa tchito pake paja chifukwa aliyense-anali ku nyoza Mulungu. Ndinaganiza mosiyananaye: uyu munthu anali paja kudalitsa pa tchito pake ndi ku sintha malowo! Tingasithe ziko lathu la pansi.

Ndapanga ganizo lakuti pamene Mulungu afuna kudalitsa anthu, makamakanso afuna yise anthu – anthu ake, bana bake – tidalitse anthu. Muli nawo ulamuliro wa uzimu. Dalitsani!

Atate wanthu aku mwamba afuna kuti titengeko mbari, ti sebenzere pamodzi, ndi iye mu tchito yake

yakuwombola anthu. Tinga dalitse anthu ndi machilitso ndi kuwombola komanso tinga dalitse anthu ndi mau. Ndise anthu Mulungu asebenzetsa mkudalitsa dziko lapansi. Iyi ndi danga ndi tchito!

Mwaichi, kwa ine, kudalitsa ndi kukamba chifunilo cha Mulungu pa umoyo wa anthu ndi zochitika zao m'chikondi, ndi maso otseguka, m'kufuna, ndi ulamuliro ndi mphanvu, kuchokela mu mzimu wanthu wozazidwa ndi Mzimu Woyela. Mwachidule, kudalitsa ndi kuchita mwa chi khulupiliro kulankhula zomwe Mulungu afuna zichitike pa anthu ndi zomwe apitamo. Tikakamba malingaliro ya Mulungu, timasula ku khoza kwa ke kuti ku sinthe zinthu kuti zikhale momwe iye afunila.

Ndipo kumbukilani – ndise wodala chifukwa tima dalitsa.

GAWO LA CIWIRI:

Mochitila

ZOCHITA ZINA ZO FUNIKILA

Lekani kamwa koyela kakhale umoyo anu

> *Ndipo dalitso ndi kutembelera zichokela pa kamwa pamodzi. Abale ndi alongo ichi sichabwino! (Yakobo 3:10, NLB)*
>
> *Ngati ukamba zabwino osati zachabechabe, uzakhala ngati kamwa kanga. (Yelemia 15:19b, RSV)*

Ngati ufuna kukamba zifunilo za Mulungu pa banthu, ndiyekuti ufunikila kuleka kukamba mau achabechabe – kapena yoyipilatu.

Funsa M'zimu Woyela zokamba

Vundulani m'zimu wanu (kupitila mkupembeza kapena kulankhula malirime). Funsa M'zimu Woyela kuti

uzindikile chimene chikondi cha Atate pali uja munthu omwe ufuna kudalitsa chifuna. Pemphera motele:

> *Atate, n'chiyani chomwe mufuna kuti chikambiwe? Chonde ndipatseni liwu la dalitso la uyu munthu. Ndingamulimbitse bwanji kapena kum'tothoza?*

Kudalitsa kusiyana ndi ku pemphelerana

Anthu ambiri anapeza kuti ndi chovuta ku mphunzila kukamba madalitso. Chifukwa cha ichi amayamba 'kupemphelera', kupempha Atate kuti adalitse. Ngakhale kuti ichi chili bwino, dalitso lo kambidwa m'menemu ndi pemphelo, ndipo ndichofunikila kudziwa kusiyana kwake. Kulankhula kapena kunena madalitso sikuma tenga malo a pemphelo kapena kupumphelerana, koma ndi paunzawo – ziyenera kupezeka pamodzi.

Wolemba a Roy Godwin ndi a Dave Roberts m'buku yawo *Kuthiilidwa kwa Chisomo* anazilongosola izi motele:

Pamene tidalitsa, timamuyangana munthu m'maso (ngati nzomwe zichitika) ndikukamba kwa iye mwachitsanzo, tingakambe kuti tele, 'ndiku dalitsa mu zina la Ambuye, kuti chisomo cha Ambuye Yesu chikhale pali iwe. Ndikudalitsa mu zina lake kuti chikondi cha Atate chikuzungulire ndi kukudzadza; kuti uziwe mkati mwako kuti akulandila ndi kukondwela nawe mokwana. Akulandira ndi kukondwela nawe.'

Ona mau yoyimirila iwe 'ndi'. Ndi amene ayimilira iwe ndi kuka mba dalitso mzina la Yesu pa munthu uja. Sindinapemphele kwa Mulungu pa dalitso koma nda lankhula dalitso kusebenzetsa ulamuliro Jesu atipatsa kunena dalitso pa anthu kuti abwere awadalitse.

Usaweluze

Usaweluze kuti munthu uyu afunika dalitso kapena iyayi. Dalitso yazoona, yokambidwa pa munthu kapena pa chinthu, imakamba zimene Mulungu awona pa anthu anja. Chimene Mulungu awona

simaonekedwe awo panthawi ija, koma mwamene afunikila kuti akhaliremo.

Mwachitsanzo, Mulungu anatcha Gidionikuti *'mzibambo wa mphanvu alibe mantha'* (Oweruza 6:12) pamene, panthawi ija, sanali telo! Yesu anatcha Peturo*'mwala'* (Mateyo 16:18) akalibe kukhala ndi 'papewa' yo nyamula zofunikira za anthu ena pa iye. Kupitiliza, tiwelenga, *'Mulungu … amapatsa umoyo ku akufa, ndi kuyitana zinthu zimene sizilipo monga zilipo'* (Aroma 4:17). Ngati tinvesentsa ichi, chizachotsa mkalidwe wanthu wa 'ku weluza'kuti kapena muntu ndiwonera dalitso kapena iyayi.

Aja anthu amene sayenela dalitso, ndiyo amene ayifunitsitsa. Anthu amene adalitsa iwo osayenela alandila madalitso yaakuku pambuyo pache.

Chitsanzo cho wonetsela

Ganizilani pali munthu zinalake Fred emwe ali ndi vuto ya kumwa moba. Mkazi wa Fred Sali wokondweranaye, mwinamwache apemphela motele: *'Mulungu dalitsaniFred. Lekani asiye moba ndipo ayambe kuni*

nvelera.' Koma chidzakhala champhanvu kwambiri kukamba motele:

> *Fred, ndikudalitsa m'zina la Yesu. Leka chifunilo cha Mulungu mu umoyo wako chichitike. Leka ukhale munthu mwamuna ndi tate womwe Mulungu anakupanga kuti ukhale. Ndikudalitsa ndi chimasuko ku kuti usiye moba. Ndikudalitsa ndi mtendere wa Klistu.*

Dalitso yoyamba yatenga vuto ndi kuyitula m'manja mwa Mulungu. Siyitengako mbari yiliyonse – ndi ya ulesi. Ndiponso ndiyachiweruzo ndi yo ziyeletsa-yeka, ndi kuyangana pa chimo ya Fred.

Dalitso ya chiwiri inatenga mbali pa kuganizilapo ndi chikondi. Siyachiweruzo koma iyangana mwamene Fred angakhalire osati mwamene aliri. Tsopano apa ndinanvera wina akunena kuti Satana adziba mazina yanthu ndi zimene tingakwanise kuchita koma amati-yitane ndi chimo lanthu, pamene Mulungu aziba machimo yathu koma atiyitana ndi mazina yathu yeni-yeni ndi zimene tingakwanitse kucita. Dalitso yachiwiri ikamba pa zimene Mulungu andandamika

ndi kufuna. Yiwonetsa mtima wa chipulumutso wa Mulungu. Kumbukilani, Mulungu amkonda Fred.

ZOCHITIKA ZOMWE TINGAKUMANE NAZO

Ndine omphunzira wa dalitso. Pamene ndinayamba, Sindinaziwe modalitsira ndipo sindinali ndi chilichonse chonthandiza. Mwamsanga-msanga ndinazindikila kuti kuli zochitika zambiri, tsopano ndifuna kukupatsani zochita izi. Mungachite izi kulingana ndizomwe zikuchitikilani, ndi kulingana ndi zomwe mukhulupilira kuti M'zimu Woyela afuna inu kuti mukambe. Ichi chizafunika kuchitanthawizonse, koma nchoyenela.

Kudalitsa iwo okunyozani ndi kukutembelerani

Zaka zambiri za ku mbuyo uko, watchito wina emwe anasiya kusebenza nase anabwela ku nyumba kumwa chakumwa ndi kulayira. Zo khulupilira zache zinali za achipembezo cha M'badwo Watsopano kapena kuti New Age – monga kuti 'zabwino mkati', ndi zina zotele. Pomwe tinali m'khani, anati m'matchito

yawiri yakumbuyo yomwe asebenzamo, yanagwa pomwe iye atasiya kusebenzamo sindinali. MKlisitu kwa nthawi yayitali panthawi iyo, koma ngakhale zinali choncho ndinazindikila kuti yanali matembelero yamene yanali kubwela. Ndinanvera mantha mwapango'no chabe ndipo m'maganizo yanga, ndinakana kuzilandira. Koma sindina pite patsogolo kumdalitsa iye. Pakumpempha kuti ndipemphele zinali mumtima mwanga, sembe ndinalakhula zotele:

> *Deborah (sidzina lake), ndimanga zochita za unfiti muumoyo wako. Dikudalitsa muzina la Yesu. Ndi lankhula kuti ubwino wa Mulungu ukhale paliiwe. Leka malingaliro ya Mulungu mu umoyo wako yachitike … Ndidalitsa zopasa zako, leka zidalitse tsogolo ya wokulemba tchito ndi ku bweletsa ulemelero wa Mulungu. Ukhale mzimayi wodabwitsa wa Mulungu yemwe anafuna kuti ukhale. Muzina la Yesu, amen.*

Kudalitsa okupweteka ndi wokukana

Nthawi yina ndina pemphelera m'zimayi anali kuvutika m'maganizo ndi ndalama pomwe mwamuna

wake adamusiya. Ndinamfunsa ngati angamukhululukire. Chabwino chinali chovuta koma, kwa nzimayi uyu, anakwanitsa kumkhululukira. Ndipo ndi na m'funsa ngati angadalitse mwamuna wake. Anadabwa pango'no, koma anali wokonzeka kuyesa. Ngakhale kuti mwamuna wake sanali naye, ndi na m'sogolera motele:

> *Ndiku dalitsa mwamuna wanga. Leka zifunilo za Mulungu zonse pa umoyo wako ndi chikwati chako zichitike. Leka ukhale munthu, mwamuna ndi tate yemwe Mulungu afuna kuti ukhale. Chisomo ndi ubwino wa Mulungu ukhale ndi iwe. Muzina la Yesu, amen.*

Poyambe chinali chovuta, koma anagwira mtima wa Atate ndipo mzozo wa Mulungu unagwa. Tonse tinalira pomwe Mzimu Woyela unali kulakhula naye ndipo, ndikhulupilira, kwa mwamuna wakenso. Njira ya Mulungu sinjira yathu.

Kudalitsa mzochitika zimenezi kufunika kukhala olimba – kulemekeza, ngakhalenso – ndipo ngati Klisitu.

Kudalitsa osayenela ndi mtima wa Mulungu – Ndiye zimene achita, tingakambe telo. Ganizilani kawalala uja anapachikidwa pa mtanda naye Yesu, kapena mzimayi anagwida chigolo. Nanga imwe na ine?

Dalitso 'siya dziko lapansi' ndipo siyiri monga ganizo – sichinthu chakuti anthu amene apita muzobaba amafuna kuchichita. Koma m'njira ya Mulungu, yimachilitsa wodalitsa ndiponso nayiye wodalitsidwa. Yimachotsa ululu woyipa wa kubaba, bwezela, kukanilira ndi ukali, zimene zimawononga thupi lanu ndiku dulitsa umoyo wanu.

Iyi ndi kalata yomwe ndina landila lomba apa kuchokela kwa Denis:

> *Mwezi yitatu yapitapo ndinali kulakhula ndi m'bale wanga pa lamya. Sinimakambitsana naye kwanthawizambiri pakuti akhala ndi kugwila tchito ku mzinda wina.*
>
> *Pomwe tinali pafupi kutsiliza kukambitsana kwaubwenzi, ndinamfunsa ngati kuti ndingadalitse malonda ake yomwe anali kutsogole ndi*

mkazi wake. Sanayakhe bwino. Anali ndi mwano ndipo analakhula zomwe zinanikhumudwitsadi, ndina ganiza kuti mwina ubwenzi wathu unathelatu. Ngakhale choncho, m'masiku ndi m'masondo yo tsatila, pomwe n'nalu kuchita zanga, ndinasebenzetsa zochita za mu Mphanvu yo dabwitsa ya Dalitsokulakhula chisomo cha Mulungu pa malonda ya m'bale wanga. Nthawizina ndina chita izi kawiri kufikila katatu pa tsiku limodzi. Tsopano, patapita mwezi itatu, pomwe kunatsala tsiku limodzi kuti tsiku la Khisimisi ifike, m'bale wanga anatuma lamya kwaine monga ngati palibe chinachitikapo pakati pa ife. Ndinakhala odabwa pali zimenezi ndi ubwenzi wake ndipo panalibe ukali uliwonse pakati pathu.

Mphanvu yodabwitsa yo dalitsa zomwe zichitika kunja kwanthu imasebenzadi… Ambuye alemekezedwe!

Kudalitsa iwo wokuyambani

Chimodzi mwa vinthu votikalipitsa kwa ena a yisendi

ngati anthu achita vozikonda, kusatiganizira kapena zinthu zonama za pamsewo. Zimachitika nthawi zonse. Mau yomwe siyali yauKlisitu yangabwere munzeru ndikuchoka pa kamwa mwa pango'no chabe. Zikachitika zomezi, titembelera wina emwe anapangidwa ndi Mulungu emwe Mulungu akonda. Mulungu angamkhalire kumbuyo munthu uja.

Nthawi yina pomwe zichitika izi, yesani kudalitsa wosebenzetsa miseu ena, m'malo mokamba mau yoyipa:

> *Ndidalitsa mzibambo wachichepele emwe wanijumphira (kunama pam'ndandanda wa wanthu). Ndilakhula chikondi chako pa iye, Ambuye. Ndimasula ubwino wako pa iye ndi zofuna zako zonse pali umoyo wake. Ndidalitsa m'nyamata wachichepele ndipo diyitana zomwe iye afunika kukhala. Lekani afike mwa m'tendere kunyumba ndipo akhale dalitso ku banja lake m'zina la Yesu, amen.*

Kapena naulemu pango'no:

Atate, ndidalitsa oyendetsa motoka iyi, m'zina la Yesu. Lekani chikondi chanu chimtsate ndi kumpitilira ndi ku m'manga!

M'modzi owerenga wanga anakamba izi zosangalatsa:

Chimene ndaona ndi chakuti dalitso yandichinja. Sindingadalitse anthu omwe andikalipitsa, mwa chitsanzo, ndiponso ndikukamba – kapenanso kuganiza – maganizo yoyipa pali iwo. Icho sichingakhale bwino. M'malo mwake ndiyanganila zabwino zochoka m'dalitaso yanga… – Jillian

Nthawi imodzi ndinali ndi mzanga dzina lache John emwe adaniyitana kuti ndipemphelere kukangana kwa pa banja komwe kunabwera chifukwa cha chuma chopatsiwa. Kukangana uku kunapitilira ndipo kunafika poyipa ndinayikapo ganizo yakuti m'malo mopemphela, tidalitse zomwe zinali kuchitika.

Tidalitsa zochitika za chongo ichi paza chumachi mzina la Yesu. Tikangananawo mpatuko, mpikisano ndi ku gwebana ndi ku masula chilungamo ndi chilinganizo ndi ku khululukilana. Pamene

tidalitsa zimezi, tiyika pambali maganizo yathu ndi zomwe tifuna ndipo timasula Mulungu kuti achite zimene afuna pali mpatuko wa chuma cho patsidwa ichi. Muzina la Yesu, amen.

Mumasiku yang'ono chabe khani inatha bwino-bwino.

Ndikonda zimene wina owerenga wanga anakamba anati:

Ndadabwitsiwa ndi kufulumila 'nthawi yoyakh-idwa' yimene ndaona mu ku dalitsa ena. Chili monga Ambuye ndi okonzeka kuyenda m'chikondi ku anthu ngati timasula ma pemph-elo ya madalitso kwa anthuwo – Mbusa Darin Olson, Junction City, Oregon Nazarene Church

Dalitso ndithudi linga sinthe chalo chathu.

TIDALITSE, TISADZITEMBELERE TEKHA

Kuzindikila ndi kuwononga matembelero
Kodi maganizo aya awoneka chiwoneke wokene bwanji: 'Ndine woyipa, sinilankhula, sindioneka bwino, ndiganiza mochebwa, kulibe wondikonda, Mulungu sanganisebenzetse, ndine wochimwa…'? Kulimaboza yambiri yamene satana amalengesa kuti tiziyakhulupilira.

Ndili ndi m'zanga womwe amachita zomwe izi nthaizonse ndipo chimandi kwiyisa. 'Iwe mkazi wopusa, Rose (sidzina lake). Wawononganso. Sungachite chilichonse bwino…'

Osakamba kapena kulandila matembelero amenewa! M'malo mwake, zidalitse.

Ndikumbukila zinachitika mu guru yamapepmphere yina. Ndina zindikila mzimu wopandapache

pa umoyo wa m'zimayi wina yemwe anabwera kumapemphelo. Pakupemphela, anati, 'sindilakhula.' Ndinamfusa kumene ananvera zomwezo. Ndipo anandiuza kuti makolo ake ada muuza zimenezi. Chachisoni … ndipo chichitika kwambiri.

Ndina m'sogolera m'njira iyi:

> *Muzina la Yesu, ndikhululukira makolo anga. Ndizikhululukira ndekha. Ndipwanya mau yamene makola anga ananena pali ine. Ndiri ndi maganizo ya Yesu Kilisitu. Ndine wochenjera.*

Mwapafupifupi tinapitikisa mizimu wakukaniwa ndi kupandapache, ndipo ndina m'dalitsa ndi kulakhula madalitso kwa iye kuti ndi mwana wa mkazi wa mfumu Mulungu, kuti ndiwofunikila kwa Mulungu, kuti Mulungu amusebenzetse m'kudalitsa ena, kubweretsa machilitso ya m'maganizo ndi chiyembekeze kwa ena. Ndi m'dalitsa cho limba.

Pang'ono pang'ono anayalandila madalitso aya. Anayamba kung'anipila. Sondo yotsatila anadzafo-

tokoza ubwino omwe unachitika pa iye. Tinga sinthe chalo chino.

Aliyense angachite zimenezi. Baibulo ndiyo-dzadzidwa ndi zimene Mulungu afuna pa anthu ake ndipo tinga lakhule zimenezi ku anthu.

Ndifuna ku kuwonetsani chitsanzo china. Ndinapempheleram'tsikana wina emwe anali ndi vuto ya m'mimba. Pomwe ndinali ku pemphela, M'zimu Woyela anagwa pa iye ndipo anagwa pamene ziwanda zinamsiya. Zonse zinalibwino pa masiku yang'ono ndipo kuwawa kuja kunabwelera. 'Nchani, Ambuye?' anafunsa. Anaganiza kuti Mzimu Woyela wuli kum'butsa kuti nthawi zina kumbuyo uko, pomwe adali ku msokhano, wina adati kuli iye kuti aphike bwino nkhuku ngatisiyapo wina adzadwala. Adati safuna kudwala pa masiku yang'ono (nthawi ya msonkhano), koma zikapita zimenezo sazdaikako nzeru. China tenga iye kupwanya mphanvu yamau yaja yachabechabe, ndipo anakhalanso bwino.

Kudalitsa kamwa kanu

> *Ndibalitsa kamwa kanga kuti kakambe zabwino osati zoyipa, ndipo kuti ndikhale kamwa ka Ambuye. (yachokela muYeremia 15:19)*

Zoziziswa zambiri za Yesu zinalikuchitika m'kukamba. Mwachitsanzo, *'Zipita; mwana wako alindimoyo'* (Yohane 4:50). Ndiye chimene ndifuna. Nchifukwa chake ndidalitsa kamwa kanga ndikusamala zochoka m'kati mwake.

Ine ndi m'kazi wanga tinali kukhala mu nyumba yaalendo ku Noumea. Tinali kunvera kamwana kulira kosaleka usiku onse. Patapita usiku ungapo, mkaziwanga ana pita komwe amayiwache analiri kukawafunsa kuti nchani chinali ku chitika. Mzimayi sanaziwe chilichonse koma anati a dotoro ampatsa mankhwala mwana koma siyanali kugwira ncthito. M'kazi wanga anafunsa ngati kuti anga mpepkelre mwanayo ndipo amayi ake anavomera, ngakhale kuti sanakhululupire. Tsopano mu chitundu cha m'tundu wa chi French chimene nenzerikuzibako pang'ono, ndinapemphelara mwana ndi kulakhula

m'chikhululupiro pa mwanayo, kuti adzagona bwino 'gona ngati mana'. Ndipo anachita.

Kudalitsa maganizo yako

Nthawi zambiri ndimakamba kuti,

> *Ndidalitsa maganizo yanga; ndili ndimaganizo ya Klisitu. Chifukwa chake ndiganiza zoganiza zake. Lekani maganizo yanga yakhale malo yoyela momwe M'zimu Woyela adzakondwera kukhalamo. Lekani yalandire mau yakuziwa ndi nzeru ndi chivumburutso.*

Kuchokela nthawi ndi nthawi, ndinakhala ndili kuganizilapo pakuyela kwa maganizo yanga, ndipo ndinapeza thandizo iyi. Ndimadalitsanso zoganiza-ganiza, kuti zisebenzedwe ku ubwini wosati kuchoipa. Ndinali kuvutika ndi zoganiza-ganiza zanga tsiku lina – yanali kuyendayenda mmalo yosiyanasiyana yomwe sindilikufuna kupita – ndipo Mulungu anayika ganizo pali ine nati, 'yangana m'zoganiza-ganiza zako Yesu alikuchita zoziziswa … *ndipo zione iwe wekha kuzichita zomwezo.' Ndapeza kuti chimase-*

benza bwino kuganizila pali chabwino' (Afilipo 4:8) m'malo mwakuganiza kusaganiza pali chilichonse! Ndipo kudalitsa maganizo yako ndizoganiza-ganiza chithandiza kwanbiri pa kukhala woyera.

Nthawi yina pamene sindinali kunvera bwino pakulephela kwa umoyo wanga wakuganiza, mau yamunyimbo yakale yanabwe mumtima mwanga:

Khala masomphenya yanga,
O Ambuye wa mtima wanga
Zonse zikhale zachabe kuchotsako iwe weka
Ndiwe maganizo yanga yabwino
msana ndi usiku
Kuwuka kapena kugona, pomwe ndiliri
ndiwe nyali yanga.

Kudalitsa mathupi yahu

Muyadziba bwinibwino malemba aya: *'Mtima wo kondwa umachita bwino, monga mankhwala'* (Miyambo 17:22)? Baibulo yilikuti mathupi yathu yamayakha kumau yabwino ndi maganizo:

Ndidalitsa thupi langa. Lero ndi phwanya
kudwala konse pa thupi panga.
Ndidalitsa kukhala bwino kwanga kwa m'thupi.

Ndinawonapo kanema kamodzi ka munthu anali kudwalitsa mtima. Mzipe wamumtima wunatsekeka. Anadalitsa mizipe zake kwa mwezi yitatu, kuyalakhula kuti yanapangidwa bwino ndiponso modabwitsa. Pamene anabwelera kwa a dotolo, chinaonekela kuti ana chilitsidwa modabwitsa pakukhala ndi mzipe wanyowani!

Ndinaganiza kuti ndiyeseko chimenechi pali thupi langa. Ndinali ndi vuto yo onogedwa ku dzuwa kuchokela ku unyamata wanga. Tsopano kuunkhalamba wanga, tomela ting'ono-ting'ono tinamela mpapewa ndi kumbuyo, tomwe tunali kufuna kutuzizilika pa mwezi yingapo. Ndinaganiza thupi langa. Pachiyambi ndina dalitsa chabe mzina la Yesu. Koma ndinawerenga chinachache chokhuza thupi (nkhanda) chimene chinasintha mwamene ndinali kuwonera. Ndinawona kuti, ngakhale ndinali kuti chinandiphimba,sindinadziwe palimbali yathupi yanga yaikulu iyi. Ndinachikambapo, koma sindina-

chikambitse. Ndipo ndikayika ngati ndinakambapo chabwino chilichonse pali ichi – m'malo mwake ndinali kudandaula. Ndinali muthu wosawonga.

Koma nkhanda ndiyodabwitsa. Imalowetsa ndi ku chotsa mphweya ndiku tsuka thupi. Yimachingiliza thupi ku matenda yomwe yamafuna kulowa mthupi ndipo yimazichilitsa yeka. Chimati phimba ndiku chingiliza zamkati mwathupi ndipo yichita zimenezi bwino-bwino.

> *Yamikani Ambuye pa nkhanda yanu – manthwinya ndi zonse.Ndikudalitsa, nkhanda.*

Patapitamwezi yingapo yakudalitsa, nkhanda yanga lero yili pafupifupi kuchilitsidwa, koma chinatsegula ndi chiyambi chaku yiyamika ndiku yilemekeza. Yinapangidwa mo wopysa ndi mokoma. Mphunzirodi. Kudandaula ku pitikitsa ufumu wa Mulungu; kuyamika kumabweletsa.

Uyu umboni ochokela kwa mzanga, David Goodman:

Mwezi yapitayo ndinanva Richard kularikira pali mutu wa dalitso – mutu omwe sukalipitsa anthu – koma umene umanveka kulingana ndikumene ubwelera chotulukapo ndichakuti dalitso siyenele kukhala chinthu chomwe tipempha kwa Mulungu, koma kuti ngati Aklisitu tili nawo ulamuliro, mwinamwache zochita, kupeleka ku dziko iyi yauchimo, ngati akazembe a Yesu, kusintha umoyo wa anthu mu ufumu wa Mulungu. Tingapitenso kunja ndiku dalitsa mu umoyo wawo, ndiku vumbulutsa Klistu kwa iwo panthawi imodzi.

Ganizo liribwino ngati wina aganizila anzake, koma ganizo imeyi yikhala ngati chimwala ngati ndiganizila kuzidalitsa. Sindina kwanitsa ku chotsa ganizo yakuti sindine woyenela, kuti ndine wodzikonda, kuti ndinali ku tenga Mulungu mwa chabe. Maganizo yanga yanasintha pamene ndinawona kuti ise, ngati aKhilisitu, ndise cholengeda cha tsopano, obadwa mwatsopano ndi kulengedwa ndicholinga cha Mulungu. Kuti ngati ni choncho, thupi tili nayo

tsopano yifunikila kuyisamala bwino ngati yamtengo wapatali – ndise tsopano, monga ziliri, kachisi yo khalamo M'zimu Woyela.

Izo zakambidwa, ndinayamba kuyesa yesa pang'ono kufuna kudziwa – tsiku yili yonse ndi-kauka, ndinali kudalitsa mbali ya thupi yanga, ndi kuyiyamika pakasebenzedwe kake; yita-mandidwe pa nchito yabwino. N'nali kuyamikira vimbombo vanga mwamene visebenzela, pa tchito zosiyana-siyana zimene zigwira ndi zina zonse. Ndinali ku yamika minyendo yanga pa kusalema kuyenda ndi kuyendisa, pakuse-benzera pamodzi. Ndinayamika ziwalo za m'thupi zonse pakusebenzela pamodzi bwino. Chachilende chinachokamo chimodzi ndi ichi.

Chifukwa ndinavera bwino mthupi ndi mzeru, Maganizo yanga ku zo wawa zomwe ndinali kunvera pansi pa dzanja langa zinatha – ukali omwe unayokeka kuti uli m'mafupa chimene chinalikufunikila kuzolewa nthawi ndi nthawi kuti kuwawa kulekeko pang'ono. Ndiyangana pali mbali iyi,kutamanda thupi yanga pa

mphanvu yodzipoletsa, kulimbikila kuti yipambane zonse zimene ziponyedwa kwa iye, pathandizo yimene ziwalo zina zipeleka pakupoletsa chiwalo china. Panapita chabe masondo atatu pamene ndinauka ndinavera kuti kuwawa konse kudzanja langa kwaleka kuwawa; kuti kuwawa kwathelatu ndipo sikunabwelerenso.

Ndinazindikila kuti pamene kuli nthawi ndi malo ya phatso yamachilitso kuyisebenzetsa mwa chikhulupiliro kuti ena apezepo phindu, kulinso njira yina yotseguka kwa yise ngati anthu kuti tisebenzetse mphatso zamachilitso kwa yise tokha. Ndiphunziro yakuzichepetsa, kuti tiyembekezele zimene Mulungu atipatsa ku mathupi yathu ya tsopano, kuti tipite mchiyembekezero munjira ya tsopano ndi ya umoyo.

Kudalitsa nyumba yanu, chikwati ndi ana

Nyumba yanu – dalitso yoyenela nyumba

Ndi nzeru yabwino kudalitsa nyumba yanu ndipo ndi dalitsanso dalitso kamodzi pachaka. Kudalitsa

malo womwe mukhalamo kufunikila kusebenzetsa ulamuliro wanu mwa Yesu Klistu ku yikiwa ndi kuyeletsa malo kwa Ambuye. Ndikuyitana M'zimu Woyela kuti abwere, ndi kulamulira zonse zomwe siziri za Mulungu kuti zichoke.

Nyumba njelwa kapena sichipupa chabe – ili ndiumuthu nawo. Monga muli ndi danga yolowa m'nyumba tsopano, winanso alindi ndi danga yolowamo m'nyumba, kapena katundu yanu, musanabwere inu. Zinthu zingakhale zinalikuchitika mu malo aja zimene zingabweretse dalitso kapena matembelero. Ngakhale zingachitike zotani, ndiulamuliro wanu wumene wuzapanga zochitika mu uzimu kuchokela tsopano. Ngati mulizochitika zochoka kumbuyoko za ziwanda, mufunikila kudziba – ndipo chili kuli imwe kuzi tulutsa ziwandazo.

Komanso mufunikira kuzindikila ndiziwanda zotani zimene mosadziwa mungazizipatsa khomo. Mulindizinthu zojambula zisali za umulungu, kapena zowumba, mabuku, nyimbo kapena ma DVD? Ndi m'ndandanda otani wapa kanema ya vikope (TV)

yomwe muvomekeza? Kodi muli chimo munyumba mwanu?

Iyi dalitso yosavuta yomwe mungakambe pamene mulikuyenda m'zipinda za m'nyumba mwanu chipinda ndi chipinda:

Ndidalitsa iyi nyumba. Ndilankhula kuti nyumba iyi ndiya Mulungu, ndiyiyeletsa kwa Mulungu ndi kuyiyika kwa Yesu Klistu ngati mwine wake. Ndi nyumba ya madalitso.

Ndi mphwanya tembelero yiliyonse muno m'nyumba ndi mwazi wa Yesu. Nditenga ula-muliro pali mizimu yiliyonse yoyipa mzina la Yesu ndiku lamulira kuti uchoke lero ndipo usakabwerenso. Ndichotsa mzimu ulionse wa kukangana, mpatuko ndi ku sagwirizana. Ndi chotsa mzimu wa kusauka.

Bwera Mzimu Woyela utululutse zonse zimene sizako. Dzadza nyumba yino ndi kupezeka kwako. Leka zipatso zako zibwere: chikondi,

> *chimwemwe, mtendere, chifundo, kudekha, ubwino, kuzichepetsa, kukhululupirika ndi kuziletsa. Ndidalitsa nyumba ino ndi mtendere wotayikila ndi chikondi chokhalilira. Lekani onse amene abwera kuno kuno azindikile chipezeko chanu ndi ku dalitsidwa. Muzina la Yesu, amen.*

Ndayenda kuzungulira molekezela katundu yanga, kuyidalitsa ndi pauzimu kuyika mwazi wa Yesu kuti uchingilize nyumba, ndi anthu mkati, ku choipa chilichonse ndi ku ngozi zochitika zekha.

Kudalitsa chikwati chanu

> *Tilindi zikwati zina zomwe timadalitsa kapena tili ndizikwati zina zomwe timatembelera.*

Pamene ndiwelenga mau aya poyamba mu *Mphanvu ya Dalitso* yolembedwa ndi a Kerry Kirkwood, n'nali odabwa pang'ono. Kodi izi ndizoonadi?

Ndachipatsanso ganizo kwambiri, ndipo ndikhulupilira kuti mau awa ndiyachoonadi kwa kukukulu – kusakodwa kulikonse mchikwati chathu n'chifukwa

chakusachidalitsa! Pakudalitsa, timalandila dalitso yoyikidwa ndi Mulungu yathu mo kwana – kuyikapo umoyo wautali ndi maubwenzi ndi ya thanzi. Tikhala wotengako mbali, kapena wosebenza naye, ndizimene ndi womwe tidalitsa.

Yanganani pa matembelero. Azimuna ndi Azimai zibanani bwino-bwino. Tiyaziba yonse mabani yo funda. Kodi m'makamba chonchi? Kodi zachoncho zinakambiwa pali inu? 'Siumanvelera', 'Chikumbumtima chako nchoipiratu'. 'Siungamphike', 'Ulibe chiyembekezo chilichonse…' Zikakambiwa kabili-kabili, mau yachoncho yakhala matembelero ndipo yazoona.

Osatembelera, dalitsa. Kumbukila, ngati utembelera (kukamba mau yakufa) siuzalandila ma dalitso ya Mulungu amene akufunila iwe. Choipa kupambana ichi, kutembelera kumatikhudza kupambana emwe tingazitembelera. Chingakhale kodi nchifukwa mapemphelo siyayakhidwa?

Kuphunzila ku dalitsa kungakhale ngati kuphunzila chitundu chatsopano – ndichovuta pa chiambi. Mwachitsanzo,

Nicole, ndikudalitsa muzina la Atate, la Mwana ndi la Mzimu Woyela. Ndimasula ubwino wonse wa Mulungu pali iwe. Leka malingaliro ya Mulungu pa umoyo wako ya chitike.

Ndidalitsa mphatso yako yakukumana ndi kukukonda anthu, mphatso yako ya kulandila alendo bwino. Ndidalitsa mphatso yako yomwe yilenga kuti anthu azinvera bwino. Ndi lankhula kuti ndiwe Osunga anthu wa Mulungu, kuti uzi-landila anthu momwe iye afunila. Ndikudalitsa ndi mphanvu yakuchita zimenezi ngakhale mzaka zako zotsilizira. Ndikudalitsa ndiwumoyo utali wokhalabwino. Ndikudalita ndi mafuta ya chikondwelero.

Dalitsani ana anu

Palinjira zambiri zodalitsilamo mwana. Ndimamdalitsa m'zukulu wanga motele, alindizaka zinai (4):

Ashley, ndidalitsa umoyo wako. Leka kuti ukhale mzimayi wabwino wa Mulungu. Ndidalitsa nzeru zako kuti zikhale za ngwiro ndikuti wukhale wanzeru ndi kuzindikira m'zoganiza

zonse. Ndidalitsa thupi lako kuti likhale la ngwiro mpaka ukakhwatiliwe ndi ku kukhala wathanzi ndi olimba. Ndidalitsa manja yako ndi mendo yako kuti yachike ntchito yimene Mulungu anayapangila kuti yachite. Ndidalitsa kamwa kako. Leka kazikamba mau ya zoona ndi chilimbitso. Ndidalitsa mtima wako kuti ukhale wodzipeleka kwa Mulungu. Ndidalitsa emwe adzakhala mwamuna wako ndi tsogolo ya myoyo ya bana bako ndi kulemera ndi chigwirizano. Ndikonda zonse zako, Ashley, ndipo ndine wonyada kukhala mbuya wako.

Komadi, pomwe mwana avutika-vutika munjira yina tingaphunzile bwino-bwino. Ngati apeza mavuto yakuphunzila bwino ku sikulu, tingadalitse nzeru zawo kuti azikumbukila zomwe aphunzila ndi zili m'maphunzirowo; ngati alikubavuta, tingabadalitse kuti akule mu nzeru ndi thupi ndi kubakomela mtima anthu ndi Mulungu ndi ana ena; ndimotele.

Ndikumbukila kulakhula ndi mzimayi wina wabwino wa Mulungu pali mzukulu wake. Zonse zomwe anal-akhula pa iye zinali kuloza pali zomwe iye sachita

bwino, m'kalidwe wakusanvela wake, ndi vuto ya m'nkhalidwe wake womwe analinawo pa Sukulu. Adamutuma ku msokhano kukatenga thandizo pa umoyo wake, ndipo anabwezedwe kunyumba chifukwa cha khalidwe ya phokoso.

Pomwe ndinanvelera pang'ono, ndinamphatsa ganizo mzimayi uyu kuti alikutembelera m'zukulu wake m'kakambidwe kake ndikumuyika m'ndende ndi mau yake. Mwaicho analeka kukamba zoipa, m'malo mwache anayamba kukamba kum'dalitsa. Mwamunawache, ambuya ake am'nyamata, anachita chimodzimodzi. M'masiku yang'ono chabe, m'nyamata uyu anasithilatu, anabwelera ku m'sonkhano ndi kuchiita bwino. Uku kukamba yakho yam'sanga-m'sanga ya mphanvu yodabwitsa ya dalitso!

Chinthu chimodzi chabwino chomwe atate angapatse ana ndi dalitso la atate. Ndinaphunzira ichi kuchokela kwaDalitso ya Atateyolembedwa ndi a Frank Hammond, ndi buku ya bwino.Popanda dalitso ya atate pamakhala ganizo nthawizonse lakuti chimodzi n'chosoba – m'bowo womwe

umakhalapo omwe palibe chingaudzadze. Azitate, sanjikani manja yanu pa ana anu, ndi am'banja ena, (mwachitsanzo,yikani manja pamuti ndi pamapewa) ndipo adalitseni kwa nthawi zonse. Pezani zinthu zabwino zomwe Mulungu adzakuchitilani inu ndi ana.

Pamene ti gawa uthengawu, ndimafunsa azibambo ndi azimai akulu-akulu, 'Ndiangati anthu muno omwe atate awo anawayika manja ndikubadalitsa?' Ndianthu ango'no omwe amanyamula manja yawo. Ndipo ndi mapindimula funso: 'Ndi anthu angati muno omwe atate awo sanabayikepo manja ndiku ba dalitsa?' Pafupifupi aliyense amanyamula manja yawo.

Ndipo ndimafunsa kuti ngati angandivomekeze kuti ndi khale ngati tate wawo pa mzimu pa nthawi iyo – woyikapo wina – kuti, mu mphanvu ya M'zimu Woyela, ndiba dalitse ndi dalitso yomwe sanalandilepo. Yakho yimakhala yayikulu: misozi, kuwomboledwa, chimwemwe, machilitso. Zodabwitsa!

Ngati ufunitsitsa dalitso ya atate, monga ndinachitila, ndiye ndikamba kuti. Ndidalitso yomwe ndatenga kuchokela mu buku ya Frank Hammond.

Dalitso ya atate

Mwana wanga, ndikukonda! Ndiwe wapadela. Ndiwe mphatso ya kwa Mulungu.Ndiyamika Mulungu pakuvomereza kuti ndi khale tate wako. Ndikunyadila ndi kukukondwelera. Ndipo tsopano ndi ku dalitsa.

Ndikudalitsa ndi machilitso ya zilonda zonse za mu mtima – zilonda zakukaniwa, kulekelelewa ndi kuvutitsiwa kumene unapitamo. Mudzina la Yesau, ndipwanya mphanvu yonse ya nkhanza ndi mau yoyipa yanakambiwa pali iwe.

Ndikudalitsa ndi mtendere wotayikila, mtendere womwe iye chabe Kalonga Wa Mtendere apatsa.

Ndidalitsa umoyo wako ndi kubala zipatso: zipatso zabwino, zipatso zambiri ndi zipatso zomwe zidzakhalilira.

Ndikudalitsa ndi ku pambana. Ndiwe mutu osati m'chila; uli pa mwamba osati pansi.

Ndidalitsa mphatso zimene Mulungu anakuphatsa. Ndikudalitsa ndi nzeru zo panga masankho yabwino ndi ku kula mwa Yesu m'zomwe afuna kuti ukhaliremo.

Ndikudalitsa ndi kupeza bwino ko tayikila, kukupanga kuti ukhale dalitso ku ena.

Ndiku dalitsa ndi ku wuza ena zauzimu, pakuti ndiwe nyali ya dziko ndi m'chele wa dziko la pansi.

Ndi kudalitsa ndi kuzama kwa kunvetsetsa za uzimu ndi kuyenda ndi Mulungu pa fupi. Siuzagwa kapena kufoka, pakuti mau ya Mulungu yazakhala ngati nyali kuli mapazi yako ndi m'saniko wa njira yako.

Ndikudalitsa kuti uziona azimai/azibambo monga Yesu analikubaona ndipo abaona.

Ndikudalitsa kuti uwone, ndikuchotsa ndi ku kondwelera zabwino mu anthu, osati zoyipa.

Ndikudalitsa kuti upeleka Mulungu komwe usebenzera – osati kuchitila umboni chabe, kapena munkhalidwe, komanso kuti ulemekeze Mulungu ndi ku pambana ndi luso pa ntchito.

Ndidalitsa ndi anzako abwino. Ulindi chisomo ndi Mulungu ndi anthu.

Ndikudalitsa ndi chikondi chokhalilira ndi cho tayikila, chomwe udza tumikila ena ndi chisomo cha Mulungu. Udzapeleka chisomo cha chi-tonthozo kwa ena. Niwe odala, mwana wanga! Ndiwe odala ndi madalitso ya uzimu mwa Yesu Klistu. Amen!

Umboni wa kufunika kwa dalitso la atate

Ndinasinthidwa ndi dalitso la atate. Mwamene ndina badwira sindinanvelepo uthenga otelowu kulalikilidwa. Sindinakhalepo ndi atate anga wondibala kuti alakhule mu umoyo wanga kufikira pano ndiliri lero. Mulungu ana sewen-zetsa inu a Richard, kundibweretsa pa malo yopemphela kuti ndikhale ndi atate anga a pa

mzimu olakhula madalitso ya atate pa umoyo wanga. Pamene muna nena dalitso la tate-ku-mwana, mtima wanga una tonthozendwa lero ndine wokondwela ndipo wodala. – Mbusa Wycliffe Alumasa, Kenya

Wakhalangati ulendo wautali ndiwovutitsitsa pamene ndinali kupita munjira ya matenda ya maganizo; nkhondo yomwe nda tchaya m'malo yosiyana-siyana: – m'maganizo, mumzimu, ndi m'thupi. Kuchilitsa zomwe ndinapitamo yinakhala ngati chotsegulira ndipo kunalibe kuyenda kutsogolo kwa kukulu kuposa kukhululukira atate anga – osati pavithu vimene ananichitila voipa chabe komanso pa vimene sananichitile vabwino – kusachita zabwino kwao. Atate anga sananiuzepo kuti anikonda. N'nali ndi manganizo yofatsa. Sanakwanitse kupeza mau yokamba ya chikondi, yo sungu ndi kusamala zomwe ndi ganiza – ngakhale pomwe ndina funitsitsa mu mtima mwanga kuti diyanvere.

Pamene kupitilira m'chikhululukiro ndi kupoletsedwa kwa mkati kunachotsa matenda ya

maganizo, ndikali nazo zoonetsela matenda amenewa zamthupi – chachikulu kuvuta kwa matumbo m'mimba. Anandilembelako mankhala ndi vakudya a dotolo anga koma sizinathandize kwakukulu, ndipo ndinauzidwa kuti zizathandiza chabe osati kupolesa iyai.

Mzanga wina, Richard, akhala alikundiuza nkhani ya dalitso ya atate, ndi mayankho yamene anthu anali kulandila. Chinthu china mumzimu wanga chinaitenga nzeru yomweyo. Ndinazindikila kuti ngakhale kuti ndina khulu-lukira atate anga pa m'bowo womwe anasiya, sindinautseke m'bowo uja kapena kukwanilitsa zimene mtima wanga ufuna.

Ndipo chinachitika. M'mawa mwina m'malo yodyela pomwe ndinali kudya chakudya cha m'maba, Richard analowa msapato zome atate anga sanalowe ndipo anandidalitsa ngati mwana. M'zimi Woyela anagwa pali ine nakhala nayine tsiku lonse. Chinali chopitamo chabwino ndipo ija mbali ya mtima wanga yimene wunali kulilira yinakhala ndi mtendere.

Chochokamo chimene sindinayembekezele ndichaku zija zoonekela zamatenda yanga ya m'matumbo zinalekelelatu. Manthwala ndi zakudya zomwe anandipatsa a dotolo ndina-zitaya. Pomwe mtima wanga unalandila zome unali kufuna, thupi langa linachilitsiwanso. – Ryan

Kudalitsa ena pa ku lamkhula chinenelo

Ngakhale Napatsa chitsanzo chokuthandizani m'kuyamba, ndichabwino kufunsa M'zimu Woyela kuti aku thandizeni mukhale kamwa ka Mulungu, kulakhula ndiku kumasula zomwe Mulungu akufuna kapena kuti mau ya Mulungu 'ya pa nthawi ija' (mau yoyenela yapa nthawi yoyenela). Ngati zimene zichi-tika zilora, yambitsani m'zimuwanu mkupemphela m'malilime kapena ku mpembedza.

Mungayambe m'kusebenzetsa zambiri zoonerako zilipamwamba, koma embekezelani M'zimu Woyela kuti ukutsogolereni. Vetselani ku gunda kwa mtima wake. Mungayambe cho yimilira-yimilira, koma muzaugwira mtima wa Ambuye mwa m'sanga.

Kudalitsa malo yatchito yanu

Bwelerani ku chigawo choyamba ndipo tengani chitsanzo ndinakupatsani, kuchokela mzimene ndinapitamo, mupeleke kuzimene mpitamo. Khalani osabisa pazimene Mulungu alikukuonetsani – angasinthe kaonedwe kanu. Dalitso silimonga mphanvu ya mayele. Mwachitsanzo, Mulungu sadza lora anthu kugula zimene safuna kapena kufunitsitsa. Ndipo Mulungu sadalitsa ulesi kapena umambala. Koma ukakwanitsa zimene afuna, ndiye kuti udalitse malonda yako – kuti Mulungu athandize kuyichotsa pomwe yiliri kuyipeleka pome iye afuna. Nverelani ulangizi wake kapena ulangizi wa anthu adzatuma kuli inu. Osabisala. Komanso yembekezelani kukoma mtima kwake, chifukwa akukondani ndipo afuna kuti mu kwanitse.

Ndinalandira umboni uyu kuchokela kwa a Ben Fox:

> *Ntchito yanga yogulitsa katundu yinapita m'zosithasitha zambiri m'zaka zatha zapitazi ndipo kunali kubwerela pansi kwa malonda. Ndinapita ku anthu ambiri pa tchito yanga chifukwa cha kuchuluka kwa tchito kunachepekela*

kufikila pa thawi yakuti ndiyamba kuda nkhawa ndi kudandawula.

Panthawi imodzi-modzi, m'kuyamba kwa chaka cha 2015, ndinanva a Brunton alikulaliikira pa m'ndandanda wauthenga wa kudalitsa tchito yako, malonda, banja ndi malo ena. Kufikila pa nthawi yomweyo, mapemphelo yanga yanali kuyangana palizomwezi kupemphe Mulungu kuti andithandize m'madela yamene aya. Nzeru yakukamba dalitso sinaphunzitsiwepo kuli yise, koma lero ndiyiona kuti ndiyolembewa mBaibulo yonse, ndipo ndidziwa kuti Mulungu atiyitana, ndikutipatsa ulamuliro wakudalitsa muzina la Yesu. Mwa yichi ndiyamba ku dalitsa tchito yanga – kulankhula mau ya Mulungu pali iyo ndikuyamika Mulungu pa tchitoyo. Ndinalimbikila kudalitsa tchito yanga m'mawa mulimonse ndikuyamika Mulungu pa malonda ya tsopano, kumpepha kuti atume anthu omwe ndidzachita nawo malonda.

Mu mwezi khumi ndi yiwiri (12) yotastira, tchito yinakula kwambiri ndipo, kuchokela pomwepo,

nthawi zine kuyikwanisa tchito yonse yinakhala yovuta chifukwa yinali yambiri imene yinabwela kwa yine. Ndinaphunzira kuti muli mwamene Mulungu tingasebenze naye mumatchito yathu nthawi zonse, kudalitsa tchito ndi mbali yamayitanidwe yathu yemwe tifunika kuchita. Ndipo mwayichi ndipeleka kuyamika kwa Mulungu. Ndinayambanso kuyitana M'zimu Woyela mumasiku ya tchito yanga, kumfunsa nzeru ndi maganizo yopanga-panga. Makamaka, ndimaona kuti ngati ndafunsa M'zimu Woyela kuti andithandize kugwila tchito bwino, ndimaitsiliza bwino pa nthawi yake.

Chiwoneka kuti chiphunzitso cha dalitso, ndimochichitila, ndichoyibalika m'mipingo zambiri, chifukwa Akilisitu omwe ndikamba nawo sachidziba. Kudalitsa tchito yanga lomba chakhala ngati chizolowezi, ndiponso kudalitsanso ena. Ndiyangananso kutsogolo ndi chiyembekezo ku wona zipatso mu anthu ndi zinthu zomwe ndimadalitsa kulingana ndi mau ya Mulungu ndipo muzina ya Yesu.

Kudalitsa m'malo omwe tikhalamo

Ndilikuganizira pa m'pingo – kapena maguru ena – kudalitsa momwe iwo apezeka ndi ku sebenzela.

Anthu amu …… (mome tikhala), tikudalitsani muzina la Yesu kuti mudzibe zimene afuna paumoyo wanu, kuti mudzibe dalitso liri pa aliyense wayinu, mabanja anu ndi zonse zichitika pa umoyo wanu.

Tikudalitsa nyumba yilionse mu …… (mome mukhala). Tidalitsa chikwati chilichonse ndipo tidalitsa ubewnzi uliwonse pakati pa anthu am'mabanja ya m'mibadyo yosiyana-siyana.

Tidalitsa thanzi yanu ndi chuma chanu.

Tidalitsa tchito zamanja zanu. Tidalitsa kusebenza kwabwino kwa aliyense kumene mulimo. Lekani zinthu ziziyenda bwino.

Tidalitsa ana a sukulu pama sukulu yanu; tibadalitsa kuti aphunzire ndi kunvetsetsa zimene

aphunzitsiwa. Lekani akule mu nzeru ndi m'thupi ndi kukomelewa mtima ndi Mulungu ndi anthu. Tidalitsa aphunzitsi ndi a phunzi ndikupemphera kuti masukulu yakhale malo yagwiro momwe chikhulupiliro mwa Mulungu ndi mwa Yesu chiziphunzitsiwa bwinobwino.

Tilankhula ku mitima ya anthu onse okhala muno m'malo yathu momwe tikhala. Tibadalitsa kuti akhale onvera kuyitana kwa M'zimu Woyela kuti akhale akunvera ndi kuchita zomwe Mzimu Woyela anena. Tibadalitsa ndi kutaikila kwa Ufumu wa Mulungu womwe tili nawo pano pa …… (church).

Nchodzibikilatu kuti madalitso otele awa yafuna kuti yapangiwe nkulingana ndi malo aja omwe akhalamo anthu aja. Ngati ndi malo okhalamo a limi, mufunika kudalitsa zoweta ndi minda zawo; ngati ndi malo aja emwe muli ulova kwambiri, ndiyekuti nchofunikila ku dalitsa ma londa alimomwemo kuti yaziyenda bwino kuti anthu apeze ncthito. Mpeleka dalitso kuli anthu omwe ofuna dalitso. Osada nkhawa ndi-

kuti kapena anthuwo ndiwonela kapena iyai! Anthu adzadziba komwe yachokela madalitso amenewo m'timima yao.

Kudalitsa nthaka

MuChiyambi, tiwona Mulungu kudalitsa anthu, kubapatsa ulamuliro pali nthaka ndi zonse za moyo, ndi kuzilamulira kuti zichuluke. Ichi ndiye chiyambi cha mbari yaulemelero wa munthu.

Pamene ndinali ku Kenya chatsopano yapa, ndinakumana ndi wotumwidwa ndi Mulungu wina emwe analiku tenga ana okhala m'miseu ndikuwaphunzitsa za ulimi. Anandiwuza nkhani yina ya malo ena yomwe munali ku khala a Silamu omwe anamuwuza kuti nthaka yawo ndiyotembeleledwa, chifukwa palibe chomwe chinali kumela momwemo. Otumidwa ndi Mulungu m'zangayu ndi anthu am'malo momwe anali ku khala anayidalitsa nthaka ndipo yinayambanso kubala. Ichi chinali cholangizilako pahanvu ya Mulungu yomwe yimasulidwa ndi dalitso.

Pamene n'nali ku Kenya, ndinayendanso m'malo momwe ana amasiye akhala yomwe mpingo wanthu unthandiza, kudalitsa dimba, dimba yawo, mitengo ndi zoweta zawo. (ndadalitsa mitengo zanga zazipatso ndi mayankho yanawoneka yambiri.)

Geoff Wiklund anena za nkhani ya mphingo waku Philippines womwe unadalitsa ka malo ka nthaka ka mpingo pamene kunali chilara. Nthaka yawo yekha ndiyo inalandila nvula. Alimi amfupi-mfupi anabwera kudzatapa madzi ya m'punga wayo kuchoke m'zitsime zomwe anakumba m'mbali ya nthaka yam'pingowo. Ichi ndi chinanso chozizitsa chomwe chiwonetsa kuti kukoma mtima kwa Mulungu kuna masulidwa kupitilira mu dalitso.

Kudalitsa Ambuye

Ngakhale nasiya ichi ku mathelo, nchofunikila kubwele pa chiyambi. Chimene nachiyikila mumathelo, ngakhale zilitelo, ndichakuti sichimayenela chitsanzo cho 'lakhula lingaliro kapena kukoma mtima kwa Mulungu pa munthu kapena pa chinthu'. Koma, ndiganizo lo 'panga chikodwelero'.

Tizam'dalitsa bwanki Mulungu? Njira imodzi yo chitilamo zimweyizi ndi yo onetsedwa mu Masalimo 103:

> *Dalitsa Ambuye mtima wanga … ndipo usayiwale zopezamo zake…*

Kodi zomwe myoyo yathu yipezamo mwa Ambuye nzotani? Apatsa chikhululukilo, machilitso, chibombolo, maulamuliro, akwanilitsa, kupatsaso mphanvu…

Ndipanga ngati m'chitidwe kukumbukira ndi kuyamika Mulungu tsiku liri lonse pazimene achita kupitila muli ine. Ndipo ndikumbukira ndikulabadila zonse zomwe ali kwa ine. Ichi chidalitsa iye, ndi yinenso! Mumanvera bwanji ngati mwana akuyamikani kapena kuku labadilani pali chimene mwachita kapena kukamba? Chimanvetsa bwino mtima wanu ndikuku pangani kuti mubachitile zambiri.

Mau yo tsilizila yo chokela ku wowerenga

> *Sichapafupi ku kamba bwino-bwino mwamene dalitso ya sintha umoyo wanga. M'zomwe*

ndapitamo pango'no kufika pa nthawi yino, kulibe emwe anakana dalitso ngati nampepha kuti nimpatse iye – Ndinakhalako ndi danga yo dalitsa mzibambo wa chiSilamu. Kuzipeleka ku pemphela dalitso paumoyo wa munthu kutsegula chitseko … ichi ndi chapafupi, njira imodzi yomwe yibweletsa zochitika ndi anthu mosaopysa ku Ufumu wa Mulungu. Kwa ine, kukwanitsa kupemphela dalitso cha yikaponso chida chapadela cha uzimu m'chola changa… chili ngati mbali ya umoyo wanga kale yinali yopelewera ndipo tsopano yayikidwa m'malo mwache… – Sandi

ZOCHITA

- Ganizilani munthu wina amene anakuchitani zoipa you – khululukani ngati nchofunikira, komanso pitani patsogolo ndi kuwa khululukira ndi kuwa dalitsa.

- Ganizilani vinthu vimene mumakamba nthawi zambiri pomwe tinena mtembelera wa enan kapen wa inu nokha. Kodi muzachita chiyani?

- Lembani dalitso ya yinu nokha, ya azimai kapena amuna anu, ndi ana anu.

- Kumanani ndi munthu wina ndipo khalani omasuka ku nenela pa iye. Pemphani Mulungu chivumbulutso cha chinachache cho limbitsa uja munthu. Yambani kulankhula vilivonse, mwachitsanzo, 'Ndiku dalitsa muzina la Yesu. Zolinga ndi zofuna Ambuye za umoyo wanu zichitike…' ndipo yembekezani, khalani wolezda.

Kumbukilani kuti muli ndi maganizo ya Yesu Klistu. Tsopano chinjanani, ndipo lekani uja munthu wina akudalitseni m'chinenelo.

- Mu mpingo mwanu, pangani dalitso ya wonse kuti mpite ndi ku chilitsa dela yanu, kapena dalitsani utumiki omwe mulinawo kale.

MOMWE MU NGAKHALIRE M'KLISITU

Aka ka buku kango'no kanalembedwa kwa aKlisitu. Ndikati 'aKlisitu', sinditanthauza anthu omwe akhala umoyo wabwino. Nditanthauza anthu womwe 'wobadwa kwatsopano' ndi M'zimu wa Mulungu ndipo akonda ndi ku londola Yesu Klistu.

Anthu ndi olengedwa mzigawo zitatu: mzimu, maganizo ndi thupi. Mbali ya mzimu inapangidwa kuti idziwe ndi ku kamba ndi Mulungu Woyela, emwe ali Mzimu. Anthu analengedwa kukhala ndi Mulungu, mzimu ndi Mzimu. Ngakhale zilichoncho, chimo la munthu litipatulitsa kwa Mulungu, ndikubweletsa infa ku mzimu wanthu ndiku dula khalidwe lathu pakati pa yise ndi Mulungu.

Nchifukwachake, anthu achita zinthu m'maganizo ndi mthupi mwao chabe. Mbali ya Maganizo mupezeka zoganiza, zofuna ndi zonvela. Chifukwa

chaichi zamziko lapansi chabe ndizo ziwonekelatu: kudzikonda, kumeka, kukondetsetsa zinthu wekha, njara, nkhondo, ndi kusowa mtendere wa choonadi ndi tathauzo.

Koma Mulungu alinalo njira yomboleramo anthu. Mulungu Atate anatuma Mwana Wake, Yesu, amene alinso Mulungu, kubwera pa dziko lapansi ngati munthu kuti atiwonetse momwe Mulungu aliri – '*ngati mwaona ine mwaona Atate*' – ndi kutenga pa iye yekha malipiro ya uchimo wathu. Infa yake yankhanza pa mtanda yinali yopangidwa kuchokela pachiyambi ndipo M'chipangano Chakale yinalankhulidwa yisanachitike. Analipira dipo la chimo ya anthu. Chilungamo cha kumwamba chinakwanilitsidwa.

Komanso Mulungu anamuutsa kwakufa Yesu. Yesu analonjeza kuti iwo adzakhulupilira mwa iye adzaukitsidwa kwa akufa kuti akakhale kwamuyaya ndi iye. Amatipatsa M'zimu wake tsopano, ngati choonetselako, kuti timudzibe ndi kuyenda naye masuku anthu onse tatsalanayo pano padziko lapansi.

Mwaichi tilindi chofunikila cha uthenga wabwino

wa Yesu Klistu. Mukavomeleza ndi ku lapa machimo yanu, mukakhululupira kuti Yesu anatenga chilango chamachimo yanu pamtanda ndi kuti anawukitsidwa kwa akufa, ndiyekuti chilungamo chake chizakhazikitsidwa kwa yinu. Mulungu adzatuma Mzimu wache Woyela kuti apatse mzimu wanu wa umunthu umoyo – kumeneku ndiye kutathauza kuti kubadwa kwatsopano – ndipo mudzakwanitsa kuyamba ndi ku kamba naye Mulungu m'chibwenzi – n'chifukwa chake choyamba anakulengani! Thupi lanu likafa, Klistu adza ku utsani inu kwa akufa ndi ku kupatsani thupi lina la ulemero, limene silidzafa. Nzabwino zimezi!

Pamene mupitiliza pa dziko lapansi ili, Mzimu Woyela (iyenso ndi Mulungu) azasebenza muli imwe (kukutsukani ndi ku kupangani ngati Yesu mu m'khalidwe) ndipo kupitila mwa inu (ku dalitsa ena).

Iwo amene asankha kusalandila zimene Yesu anabachitila adzapita ku chiweluzo kuli zilango zonse. Kodi mufuna chimenechi?

Ili ndi pemphelo lomwe muunga pemphele.

Mukalipemphela m'choonadi mudzabadwa kwatsopano.

Chonde Mulungu ku mwamba, Nabwela kwa imwe mu zina la Yesu. Ndivomekeza kwa inu kuti ndine wochimwa (lapani machismo yonse yanu yomwe mudziba.) Ndine wogonja ndi machimo yanga ndi umoyo ndakhala ninalinawo kombula inu ndipo ndifuna chikhululukiro.

Ndikhulupilira kuti Mwana wanu yekha, Yesu Klistu, anakhesa mwazi wake wapatali pa mtanda ndi kufa chifukwa cha machimo yanga, ndipo lero ndine wodzipeleka ku siya machimo yanga.

Unatelo mBaibulo (Aroma 10:9) kuti ngati tilakhula kuti Yesu ndi Mphulumutsi ndiku khululupira m'mitima zathu kuti Mulungu anamu utsa kwa akufa, tidza pulumutsidwa.

Panthawi yino ndikamba kuti Yesu ndiye Mwini wa moyo wanga. Ndikhulupilira kuti Mulungu anautsa Yesu kwa akufa. Panthawi yamene

yino ndilandila Yesu Klistu ngati Mpulumutsi wanga ndipo, monga momwe mau ya Mulungu yakambira, panthawi yino ndapulumutsidwa. Zikomo, Ambuye, pakundikonda kwambiri ndipodzipeleka kufa m'malo mwanga. Yesu ndiwe odabwitsa, ndipo ndikukonda.

Tsopano ndikupempha undithandize kupitila ku Mz'imu Woyela wako kuti ndikhale munthu omwe ufuna kuti ndi khale kuchokela pa chiyambi cha nthawi sichinayambe. Nditsogolere kuwokhulupilira anzanga ndi ku mpingo womwe uzasakha kuti ndikule mwa iwe. Muzina laYesu, amen.

Zikomo pakuwerenga buku lingo'noli.
Ndingakonde kuti ndilandire umboni mome
dalitso lakusinthilani umoyo wanu, kapena
umoyo wa ena omwe inu mwa dalitsa.
Chonde kambani maiyine kupitila:

richard.brunton134@gmail.com

Dalitso ndi ku lakhula zofuna za Mulungu kapena kukomela mtima pa muntu kapena pa zomwe zikuchitika.

Tikachita zimwezi mu chikhulupiliro, tiyambitsa mphanvu ya Mulungu ku sintha munthu (naise kumodzi), kapena chochitika, kuchokela pomwe aliri tsopano kufikila kome Mulungu afuna kuti apezeke.

mKlistu aliyense alindi ulamuliro ndi mphanvu zo dalitsa ena mu zina la Ambuye ndikuwona myoyo za anthu ndi zomwe zichitika pa umoyo wao kusintha. Mphanvu ya dalitso ndi ya Uzimu; ndi tchito ndi kupezeka kwa Mzimu Woyela, kubweretsa chimwemwe, mtendere, kupezabwino ndi kubala zipatso; ndi ku bweretsa thanzi, kuchita bwino ndi chichingilizo.

M'kabuku kango'noka, mudzapezamo momwe dalitso yisebenzela ndi ku phunzira mome munga dalitsile iwo wotembelera kapena wokuyambani; modalitsila akazi kapena amuna anu, ana anu, nyumba yanu ndi yinu nokha; modalitsila pa tchito panu, nthaka yanu ndi malo yomwe mukhalamo ndi anthu ena – ndiponso Mulunguiye.

Munga sinthe dziko lanu.